NEW LIFE IN JESUS CHRIST (CHINYANJA)
PUBLISHED BY BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P. O. BOX 31995, LUSAKA, ZAMBIA

File 1982

# Moyo watsopano mwa Yesu Kristu

# Moyo watsopano mwa Yesu Kristu

**NEW LIFE IN JESUS CHRIST**
(Chinyanja)

FIRST PUBLISHED
1 October, 1982

BY THE
Baptist Publishing House
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia

PRINTED BY
Baptist Printing Ministry
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia

**Writers:** Betty Ann Whitson/Helen Gilmore

5. Onetsani nchito za amene ali wokhulupirira mwa Kristu. (1 Timoteo 6:11)

Pemphero:

Tiyeni tipemphere kuti Mulungu adzatipanga kukhala mboni zace, kuyambira lero. Pempherani kuti tidzalandira cimwemwe cosatha.

3. Pemphero.

4. Kupindula muntu m'modzi yemwe athandiza kuuza ena.

5. Kutsatira citsogozo ca Mzimu Woyera. "Wakukhala mwa Ine, ndi Iye mwa iye, ameneyo abala cipatso cambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kucita kanthu" (Yohane 15:5).

6. Kuzindikira kuti mantha ndi cimo. "...ndipo ciri conse cosaturuka m'cikhulupiriro ndico ucimo." (Aroma 14:23)

7. Kuzindikira kuti munthu aliyense ndi otaika akakhala opanda Yesu monga Mpulumutsi "Ndinena kwa inu, Iaitu; koma ngati simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse cimodzimodzi." (Luka 13:5)

8. Kuphunzira kuti sikofunikira kudziwa zonse pofuna kuyesa kucitira umboni.

9. Kufotokozera kwa munthu momwe cipulumutso cinafikira kwa inu.

10. Kufotokoza kwa munthu njira yacipulumutso yapafupi.

GAWO 4: NJIRA YA CIPULUMUTSO

1. Onetsani munthuyo kuti ndi ocimwa ndi kuti ndi otaika (Aroma 3:23).

2. Onetsani kuti sangadzipulumutse yekha (Macitidwe 4:12).

3. Onetsani kuti ndi Kristu yekha amene angamupulumutse (Aroma 6:23).

4. Onetsani kuti Kristu adzamupulutsa munthu olapa ndi kukhulupirira (Luka 13:5).



## MOYO WATSOPANO MWA YESU KRISTU

MUTU WA PHUNZIRO: MKAZI WATSOPANO
Wolemba, Mrs. Betty Ann Whitson

PHUNZIRO — TSAMBA


1. KUTAYA ZAKALE....................3
2. MKAZI WATSOPANO MWA KRISTU...........7
3. MKAZI WATSOPANO KUNYUMBA............11
4. MAI WATSOPANO PAKATI PA ANTHU NDI MPINGO..............................15


MUTU WA PHUNZIRO 2: KUZAMA MWAUZIMU


5. KUPYOLERA MU KUPEZEKA KU CHALICHI...19
6. KUPYOLERA M'MAPEMPHERO..............23
7. KUPYOLERA KUPHUNZIRA BUKU LOPATULIKA..........................28
8. KUPYOLERA MUKUDZIPEREKA KWA WEKHA...32


MUTU WA PHUNZIRO 3: UMBONI WA MACITIDWE ATSIKU NDI TSIKU
Wolemba, Miss Helen Gilmore


9. MACITIDWE ATSIKU NDI TSIKU A KUNYUMBA NDI MU MZINDA......................36
10. UMBONI KUPYOLERA KUPHUNZITSA ANA....40
11. UMBONI WA MUNTHU...................45

za mu sande sukulu, W.M.U. ndi pa iye yekha.

2. Iye anali kuwerenga Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku.

3. Iye analoweza mau a ndime za Buku Lopatulika zomwe zingamuthandize kucitira umboni kwa wina aliyense za Yesu.

4. Iye anali kupemphera tsiku ndi tsiku kuti Mulungu amupatse mwai wocitira umboni ndikuti amuthandize pocitira umboni.

5. Iye adalemba maina wa abwenzi ace amene sanali Akristu ndi kuwapempherera tsiku ndi tsiku. Iye anali kucezera abwenzi amenewa. Kupyolera mu moyo wace wa ci Kristu ndi mau ace aumboni anayesa kuwatsogolera ku cipulumutso copyolera mwa Kristu. Iye anafuna kuti anthu ena akhale ndi cimwemwe mu mitima yao monga momwe analili.

GAWO 3: KUGONJETSA MANTHA

Ambiri mwa abwenzi a Cikristu a Mai Esita anali ndi manyazi kapena mantha kucitira umboni za Kristu. Nazi zinthu zina zomwe zinathandiza amai Esita kuti agonjetse manyazi ndi mantha.

1. Cikondi "Mulibe mantha m'cikondi koma cikondi cangwiro citaya kunja mantha,---" 1 Yohane 4:18.

2. Kudalira pamalonjezano a Mulungu "Iye amene ayendayenda nalira, ponyamula mbeu yakufera; adzabweranso ndithu ndi kufuula mokondwera, akunyamula mitolo yace." Masalmo 126:6

Amai Esita pamenepo anali ndi mwai wouza Bambo uja kuti Abaptist amakhulupirira kuti kuli Mulungu m'modzi; kuti Mulungu wa mphamvu zonse adalenga momwemo. Mulungu adapanga munthu kuti adzikhala ndi ciyanjano naye. Koma iye adapatsa munthu cifuniro cobvomereza kapena kukana Mulungu. Munthu adacimwa. Iye adatembenuka ndi kufulatira Mulungu. Cifukwa Mulungu ndi woyera, sakadakhoza kuyamikira macimo a munthu. Komabe Mulungu akonda munthu ndipo afuna kumupulumutsa. Cifukwa ca cimeneci adatumiza mpulumutsi, mwana wace Yesu Kristu, kudzakhala nsembe ya macimo a munthu. Kupyolera mwa Yesu Kristu timadziwa za cipulumutso ca Mulungu ca kwa ife. Ndi kupyolera mwa Yesu momwe tingathe kubwezedwa kwa Mulungu. Tiyenera kulapa macimo athu, kubvomereza Kristu monga Mpulumutsi ndi kumvera Mulungu ndi kucita nchito yace mu dziko lace. Mu njira yotere timakhala ndi ciyanjano codzaza ndi Mulungu ndi cimwemwe ndi mtendere mu dziko, ndi lonjezano la moyo wosatha ndi Mulungu.

GAWO 2: KUKONZEKERA KUCITA UMBONI

Amai Esita asanapite kukacezera banja limeneli, sanadziwe kuti Mulungu adzamupatsa mwai otani wocitira umboni kwa wina wace amene sanali Mkristu. Koma iye anali wokonzekera kukanena zomwe Mulungu anamucitira. Iye anazindikira nchito yace yaikuru ndiyo yobweretsa ena kuti adziwe Kristu monga Mpulumutsi wao.

Kodi iye anakonzekera motani kukacitira umboni?

1. Iye mwini ndi Mkristu. Iye anadziwa mu mtima mwace zomwe Mulungu anamucitira. Iye adaphunzira dongosolo la Mulungu la



MUTU 1

MUTU WA PHUNZIRO: MKAZI WATSOPANO

MUTU WA LERO: Kutaya Zakale...

MAU APAMTIMA: "Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano, zinthu zakale zapita taonani zakhala zatsopano."
2 Akorinto 5:17

(Onani: kwa dongosolo la miyezi ino, lembani 2 Akorinto 5:17 pa bolodi kapena pacipepala cacikuru).

KUFOTOKOZERA:

(Mtogoleri) - Pamene tikhala Akristu timakhala ndi moyo watsopano mwa Kristu. Monga tawerenga mu Akorinto, tiyenera kubvula munthu wa kale ndi kukhala monga olengedwa atsopano. Imeneyi ndi nchito yaikuru koposa ndipo si Akristu onse atsopano amasintha msanga njira zao. Kawiri kawiri amakhala ocedwa kuona kuti iwo alore Kristu kuonekera pa zinthu zimene acita. Mwina mwace dongosolo la maphunziro awa likuthandizani.

Tikhala tiri kuona miyoyo ya azimai awiri amene adakhala ndi makhalidwe ofanana ndi momwe muli kukhalira. Onse awiri adangobvomereza Yesu mwa cikhulupiriro. Tiwachula iwo Elizabeti ndi Veronika. Iwo akhoza kukhala aliyense wa inu.

GAWO 1:

Pamene Elizabeti anali kuyenda mseu otsi-

kira kunyumba kwace, anali okondwa kwambiri. Iye sanadikire kuuza mwamuna wace Yohane zomwe zaoneka m'mawa wa lero. Iye anadziona kuti ndi oyera ndi osiyana mkati popeza iye anadziwa Yesu monga Mpulumutsi wace. Iye anabwera mu mtima mwace ndikukhalamo, ndipo cimeneci anayenera kugawana ndi apabanja lace. Panalibe ndi m'modzi yemwe amene anali Mkristu. Iwo onse anali kutsatabe njira zakale za makolo ao.

Bwenzi wa Elizabeti, Veronika, anali kukhala pafupi ndi kumapeto a mzinda. Iye anali kuyenda kunyumba kucokera ku mapemphero a m'mawa ali okondwera mkati mwace. Iye adanena potsiriza pa msonkhano kuti, "ndiri kufuna kukhulupirira mwa Yesu ndi kumutsata Iye." Koma panalinso kusokonezeka m'maganizo ace. Iye anali kudera nkhawa kuti apabanja lace adzanena ciani. Mwamuna wace, Edward, adzakhala wokalipa ndi iye cifukwa adacoka kumunda wao m'mawa ndi kupita ku chalichi. Iye anali ndi nchito yabwino monga kalembela wa mu mzinda ndipo mkaziyo anali ndi udindo wosamalira za pamundapo. Iye adaganizira kuti sauza aliyense zakukhala Mkristu. Iye azisunga mwacinsinsi.

GAWO 2:

Yohane anali kudikira kubwera kwa Elizabeti mwaukali. Iye anabwera kucokera ku msika ndipo anali ndi njala. Panalibe cakudya comwe cidakonzedwa. Pamene anamuona alikubwera, adayamba kubweza mau mwaukali. Elizabeti mwacinsinsi adati pepani ndiphika mwa msanga cakudya, komatu kanthu kena ka padera kana citika. Mau ena onyoza adacokera kwa iye, ndipo adasiya mwa msanga. Kodi cosiyanaco ndi ciani?



PHUNZIRO 11

MUTU WA PHUNZIRO: UMBONI WAZOCITA ZATSIKU NDI TSIKU

MUTU WA LERO: UMBONI WA MUNTHU

MAU APAMTIMA: "Cifukwa cace pemphani mwini zotuta kuti akokose anchito kukututa kwace." Mateyu 9:38

KUFOTOKOZERA:

Tidalengedwa kuti tidziyanjana ndi Mulungu ndi monga zida za zotengera cipulumutso kwa azimai anzathu. Ngati ife sitikonda azimai anzathu, sitikonda Mulungu moona. Njira imodzi yoonetsa cikondi cathu kwa Mulungu ndiko kugawira cikondi cace ndi ena.

GAWO 1: MBONI

Tsiku lina amai Esita anali kuceza mu nyumba ya m'modzi wa ana a sande sukulu yace yemwe sanabwere tsiku la sande lina. Amalume amwanayo nao anali kuceza kunyumba kwa mwanayo. Pamene iwo anali kulankhulana, Amai Esita adafunsa bamboyo za ku chalichi komwe amapita. Iye adachula cipembedzo cina. Ndipo iye anati, "kodi sukulu imene muli kulankhulayi ndi ya ciani? Kodi mumaphunzitsa Buku Lopatulika?"

Amai Esita adafotokoza colinga ca kukhala ndi sande sukulu. Bamboyo adayankha, "Ine ndikadakonda kuphunzira Buku Lopatulika. Muona kuti mpingo wanga siuphunzitsa Buku Lopatulika. Kodi mpingo wanu ndi cipembedzo cina? Kodi mpingo wanu mwaphunzitsa zaciani?"

GAWO 5: KUPHUNZITSA MAKHALIDWE

Pophunzitsa makhalidwe kwa ana athu, nazi zinthu zina zomwe tifuna kuti zicitidwe mwa iwo:

1. Kulemekeza anthu ena cifukwa ca udindo ndi cuma cao.
2. Kukhulupirika m'macitidwe a tsiku ndi tsiku.
3. Khama lotsiriza kugwira nchito bwino.
4. Ciweruzo ca bwino popanga malingaliro.
5. Luntha loganizira kusiyanitsa maudindo ofunikira.
6. Cikondi comwe cimafikira anthu ena amitundu ndi mafuko ena.

Makhalidwe monga awa sangathe kumcitika ndi moyo wa munthu pa tsiku limodzi; koma mwa pang'ono pang'ono kwa nthawi ya zaka zambiri. Ana amabadwa osamvetsetsa zinthu zimenezi. Iwo amaziphunzira kucokera kucitsogozo comwe amacipeza kucokera kwa makolo awo.

Pemphero:

Lolani mai aliyense apemphere mwakacetecete kwa mphindi zocepa kuti Mulungu adzamutsogolera tsiku ndi tsiku kukuza ana ace. Funsani wina wace kuti atseke msonkhano.



Nthawi zambiri mkaziyo anali kubwezera poyankha ndipo panali kumakhala mkangano. Elizabeti adaoneka osinthika mwina mwace. Kodi caoneka ndi ciani?

Paulo, mwana wa Veronika anathamanga kukakomana ndi iye pamene anali kubwera njira yopita kunyumba kwao. Iye adamuuza kuti pali mwamuna wina amene afuna kuonana ndi mwamuna wace. Pamene iye adafika, adaona Petro bwenzi la mwamuna wace. Iye adawabwereka ndalama, ndipo iwo adayenera kuzibwezera lero. Iye adadziwa kuti analibe zokwanira ndikuti akhoza kukhala okwiya. Poiwala za zomwe zaoneka ku chalichi m'mawa adaganizira kuuza munthuyo kuti mwamuna wace wacoka ku mzinda mofulumila cifukwa abale ace alikudwala. Iye waiwala kumupatsira ndalama, koma adzabweretsa mwa msanga atangobwera. Cimene cidakawapatsa nthawi yakuti apeze ndalama zina zotsalazo.

GAWO 3:

Linali tsiku lamsika ndipo Elizabeti anali kukonzekera kutenga ndiwo zaziwisi kupita nazo ku msika kukagulitsa. Iye adakumana ndi abwenzi ace ena ambiri ndipo iwo anali kuyendera pamodzi kupita ku mzinda. Veronika adakumana nao panjira. Pamene anali kulankhulana ndikumaseka panjira, Veronika adafotokoza momwe adapusitsira Petro, koma Elizabeti sadaseke ndi anzace. Iye anali kuganizira za macimo ambiri amene ayenera kucotsedwa ngati iwo ayenera kukhala Akristu abwino.

Ndiwo za masamba zao zonse zitatha kugulitsidwa, mai wina adapita pogulitsira mowa pafupi ndi msikawo asanapite kunyumba.

Veronika adalowa mgulu la ena namugulira mowa, anaganizira kuti, "zoonadi, ndikamwako sindingapweteke, abwenzi anga onse ali kumwa." Koma pamene adayang'anitsitsa anaona kuti Elizabeti, sanagule mowa, koma anali kulankhulana ndi bwenzi.

Ena mwa azimaiwo anafunsa Elizabeti cifukwa comwe sanamwere mowa. "Inetu ndine Mkristu tsopano;" anatero alikusekerera.

GAWO 4:

Tsopano, tiyeni tiwerengenso 2 Akorinto 5:17. Monga tamva za abwenzi athu awiri Elizabeti ndi Veronika, kodi taona bwino kuti Akristu atsopano amafunika kutaya zonse za moyo wa kale zomwe ziri zaucimo? Kodi ndi zolakwa zotani zomwe Veronika adacita? Kunama, kulongolora, kusadekha, kumwa mowa, ndi zinthu zina zocepa zomwe zingaononge moyo wa Mkristu. Kodi inu muli nazo njira zina zomwe muyenera kuzisiya? Kodi ena akhoza kuona kuti ndinu osintha cifukwa cakuti ndinu Mkristu?

PEMPHERO:

Kuti mai aliyense wopezeka lero aone mu moyo wace ndi kupempha Mulungu kuti amuthandize kukhala Mkristu wabwino.



GAWO 4: KUPHUNZITSA KUYAMIKA

"Amai, onani kacilombo komwe ndakapeza," anatero, Davide.

"Inde, ndiri kuona. Ndikalanda mfuno." Amai anatero. "Kamadya nchenche ndi udzudzu, motero ndikothandiza kwambiri."

Davide anati, "koma bwanji kali kamaonekedwe osiyana?"

"Inde," anatero amai. "Koma imeneyi ndiyo njira adakapangira Mulungu, inu udziwa iye adapanga zinthu zodabwitsa zambiri ndipo amakonda zosiyana siyana. Kodi siuli wokondwa kuti Mulungu adapanga zinthu zambiri kuti ife tidzisangalala nazo?"

"Inde, ndimakonda maluwa okongola onse ndi mitengo imene tiri nayo," anatero Davide.

"Kodi mukadakonda kuthokoza Mulungu cifukwa cotipatsa ife zinthu zokongola kuti tikondwere nazo?" anafunsa amai.

"Inde ndikadatero," anayankha Davide. Anawerama mutu wace nanena kuti, "Zikomo inu, Mulungu, cifukwa ca zinthu zokongola zomwe mumatipatsa, kweni kweni maluwa ndi mitengo ndiponso kacilombo aka komwe kamadya udzudzu."

Davide anali kuphunzira kuyamikira zodabwitsa za cilengedwe ca Mulungu ndi kukongola komuzungulira. Posacedwa adzayamba kubvomereza kusiyana kwa mwa anthu cifukwa adziwa kuti Mulungu adawalenga motero.

kupereka mwayi kwa mwanayo kuti akafotokoza yekha kwa wogulitsa ndikubwezera ndalama. Ngati mwanayo sangamvetsetse kuti ndalamayo iyenera kubwezedwa, maiyo ayenera mofatsa kutsogolera mwanayo kuzindikira cimeneci.

Cimeneci ndi citsanzo cimodzi cokha ca kuphunzitsa kwa makhalidwe. Makhalidwe amaphunzitsidwe tsiku ndi tsiku mwa zocita.

GAWO 3: KUPHUNZITSA KUKHALA WOPATSA

Amai anabwera kunyumba kucokera kocezera abwenzi tsiku lina ndikunena kuti kwa "Marko mwana wa anzathu alikudwala ndipo atate ace alibe nchito. Kodi muganiza kuti tikhoza kumucitira ciani?"

Mwana wace Samueli anati, "tikhoza kumupatsa dzila. Nkhuku zathu ziri kuikira mazila ambiri tsopano." Kodi lingaliro labwino ndi liti," amai anatero.

Jane anati, "ine ndiri ndi galimoto laling'ono lomwe ndidadzipangira kucokera ku kabokosi. Mwina akhoza kusewera nako."

Amai anati, "ndiganiza akhoza kukonda kameneko kwambiri."

Mwana Petro anati, "ndimujambulira cithunzi. "Motero mwana aliyense anali ndi mbali yothandiza Marko ndikuphunzira momwe angagawirire ena. Mai akadakhoza kudzitengera zinthu yekha kukapereka kwa Marko, koma polora ana ace kugawira, anawaphunzitsa phunziro lopambana.



MUTU 2

MUTU WA PHUNZIRO: MKAZI WATSOPANO

MUTU WA LERO: Mkazi Watsopano Mwa Kristu

MAU APAMTIMA: "Lirani monga makanda alero mkaka woyenera, kuti mukakule nao kufikira cipulumutso; ngati mwalawa kuti Ambuye ali wokoma mtima."
1 Petro 2:2-3

KUFOTOKOZERA:

(Mtsogoleri) - Mu ndime yathu tawerenga kuti Mristu ayenera kutaya zinthu zambiri m'moyo wace ngati ali oyenera kuti akule mu cisomo ca Mulungu. Iye ayenera kutaya cidani, nsanje, kusankhulupirika ndi ciri conse comwe cidzaononga moyo wace wa njira yatsopano. Iye adafunika kumva mau a Mulungu ndi kuwaganizira za tanthauzo lace kotero kuti akhale wofanana ndi Kristu. Lero, tiona zinthu zina zomwe Elizabeti anacita kuti akule mu cikondi ca Kristu.

GAWO 1:

Mumasabata otsatira kulapa kwao, Veronika ndi Elizabeti anapita ku Sande Sukulu ndi ku chalichi mokhulupirika. Kamodzi pa sabata anali mukalasi ya ubatizo imene inali kuphunzitsidwa ndi mbusa. Cimeneci cinali cothandiza cifukwa iye anafotokoza zinthu zambiri zokhalira umoyo wa Cikristu ndi ciwalo ca mpingo wa Baptist.

Elizabeti anagwira nchito molimba kunyumba kotero kuti akhale ndi nthawi yodzacita nao kalasiyo ndi msonkhano wa mapemphero. Iye

sanafune kulephera. Veronika anali kuyenda mtunda utali pang'ono, ndipo kawiri kawiri sanali kupezeka kukalasiyo kapena ku chalichi pa nthawi yace. Cimeneci cidapangitsa kuti asamvetsetse zinthu zonse ndipo posacedwa adayamba kungokhala kunyumba. Iye anali ndizifukwa zambiri zomwe adaganizira kuti zinali zabwino. Kunali kutali kwambiri ndipo anali ndi nchito yambiri pa munda wace. Poonjezera, iye anali kupita kamodzi pa mwezi. Kameneka kanakakhala kokwanira.

GAWO 2:

Cinthu cimodzi coyamba comwe Elizabeti adacizindikila m'moyo wace wa tsopano cinali cimwemwe pakumva mau a Mulungu. Sabata ili yonse anali kutha kumva bwino za cikondi ca Mulungu. Za citonthozo comwe anamupatsa. Iye sanali kutha kuwerenga bwino koma anali kuwerenga kucokera mu Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku. Kawiri kawiri cinali kumutengera nthawi yaitali kuti awerenge ndime zocepa. Atatha kuziwerenga anali kuganizira za tanthauzo lace ndipo nthawi ina ya tsikulo anali kuyesa kucita monga Buku Lopatulika lamuuzira. Pamene mbale wace anali kumucezera anali kumupempha kuti amuwerengere Buku Lopatulika. Iye anali kusukulu ndipo anali kuwerenga bwino. Ndi cabwino kuti Mulungu anatumiza mau ace kuti onse awerenge ndi kuwatsata.

GAWO 3:

Elizabeti adapitiliza kukhala odabwa pa zosinthika zomwe zinali kucitika pang'ono pang'ono mu mtima wace. Iye nthawi zonse anali oyamba kuuka mbanja lace, kuuka dzuwa lisanatuluke. Tsiku kwa iye linali lodzaza



abwenzi ena." Amaphunzira kukhala osakhulupim'moyo pamene aona atate ao abwera kunyumba okhuta mowa kapena amai ao aononga ndalama pa zobvala za mtengo wa pamwamba, zomwe zikadagwiritsidwira pogula cakudya ca ana ace. Makolo ayenera kukhala okhulupirika ndi Mulungu ndi anthu ena.

GAWO 2: KODI TIMAPHUNZITSA MOKHULUPIRIKA MOTANI?

Amai ndi mwana wace wamkazi wa zaka zisanu anapita kusitolo. Iye anagula mkate, anaika ndalama pa tebulo patsogolo pa wogulitsa, amene adaiwona, koma adalephera kuichotsa mwamsanga. Amai adatembenuka kuti aone kanthu kena mu sitolomo. Ndipo adaitana mwana wace ndipo adacoka mu sitolomo. Pamene anaona m'manja mwa mwana wace podutsa mseu, mwanayo anali ndi teni ngwee m'dzanja lace. "Kodi iwe waitenga kuti ndalamayi?" Amai adafunsa. "Mu sitolo," mwana anayankha. "Kodi iyi ndi ndalama ija ndinaika patebulo?" Amai adafunsa, "inde, koma wogulitsa uja sanaifune; sanainyamule," mwana anatero. "Ndalama iyi ndi ya ku sitolo. Kuitenga ndi kuba. Tabwerera kusitolo. Uyenera kupereka ndalamayi kwa ogulitsa ndikumuuza kuti pepani ndalakwa kuti ndinatenga ndalama." Amai anatero.

Ngati mwanayo akanakhala wamkuru ndi wozindikira kutanthauza kwa kuba ndi ciani, mai uja mwina akananena kuti, "Iwe udziwa kuti kuba ndi koipa. Ngati siubwezera ndalama, ukhala ndi cikumbu mtima ndipo siukhala okondwa. Kodi ucita ciani?" Ngati mwanayo, ayankha, "Bwezerani ndalamayi kusitolo, "ndiye kuti amai akadabwerera ndi mwanayo kukaibweza,

PHUNZIRO 10

MUTU WAPHUNZIRO: UMBONI WA MACITIDWE ATSIKU NDI TSIKU

MUTU WA LERO: UMBONI KUPYOLERA KUPHUNZITSA ANA

MAU APAMTIMA: "Ndipo muziwaphunzitsa mwacangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala pansi m'nyumba zanu, ndipoyenda inu panjira, ndi pogona inu pansi, ndi pouka inu."
Deuteronomo 6:6-7

GAWO 1: COFUNIKIRA KUPHUNZITSA ANA

Kaya tiri ndi ana kapena ai, ambiri a ife tiri ozungulidwa ndi ana. Tiri ndi udindo wokonda ndi kuwaphunzitsa. Ngati Mulungu anakupatsani ana, limodzi la udindo wanu wa ukuru m'moyo ndi kuphunzitsa iwo cikondi ndi malamulo a Yesu Kristu. Kukhala Mkristu ndiko kuganizira moyo kuti ndiwo mphatso ya Mulungu. Kumbukirani kuti nthawi iyenera kugwiritsidwa mwa nzeru. Kukhala Mkristu kutanthauza kukhala okhulupirika kukhala osadzikonda, wodekha ndi wacikondi.

Koma kodi timaphunzitsa malamulo amenewa kwa ana motani? Ana amaphunzira zambiri kucokera ku zitsanzo kuposa ciphunzitso colankhula cifukwa ca cimeneci, tiyenera kukhala azitsanzo zabwino ife eni. Ana amaphunzira kunena bodza pamene amva makolo ao akunena bodza za misinkhu yao pofuna kuwalowetsa musukulu. Iwo amaphunzira kulankhula zonama pamene amva atate ao akuuza bwenzi, "sindipita ku nchito lero. Ndidauza mkuru wa pa nchito kuti ndadwala lero, koma ndiri kufuna kucezera



ndi nchito posamalira banja lace, kumunda ndi nyumba. Iye adayamba kukonda bata la nthawi ya m'mawa ndipo asanacite kali konse anali kupemphera ndi kulankhulana ndi Mulungu.

Poyamba m'mapemphero ace anali wa manyazi kwambiri ndi kukhumudwa. Iye sanali kudziwa kupemphera bwino. Ku chalichi mbusa anali kuitana Akristu osiyana siyana kuti atsogolere pemphero. Pamene iye anamufunsa Elizabeti, anali ndi mantha akuru kotero panalibe wina anamva mau a pemphero lace. Atatha mapemphero a mpingo anamufotokozera kuti anayenera kungolankhula kwa Mulungu ndipo adzamva zonse zimene adzanena. Iye anayamba ndikuthokoza Mulungu cifukwa ca ubwino wace. Tsiku liri lonse cinakhala capafupi kupemphera ndikumanena zinthu zimene anafuna mu mtima mwace. Posacedwa anayamba kupemphera opanda mantha.

GAWO 4:

M'mawa wa tsiku lina pemene Elizabeti anali kusinja cimanga anaona Veronika alikubwera. Atangotha kupatsana moni, Veronika anayamba kuuza Elizabeti kuti anaona kuti satsiliza kalasi yaubatizo. Cifukwa iye analephera kupezeka pa makalasi ambiri panali zinthu zina zomwe iye sanali kumvetsetsa ndipo anali kufuna cithandizo.

Elizabeti anali okondwa kucita zimenezi ndipo pamene onse, anakhala m'munda anayamba kufotokozera Veronika zinthu zina zomwe zinaoneka kwa iye. Iye anapeza mphamvu ndi cidziwitso ca za Mulungu cambiri pomapita ku chalichi pa tsiku lopemphera. Iye adaphunziranso njira zambiri pomuonetsa cikondi ca Kristu. Mu mtima

mwace anadziwa kuti adasoweka kumva ndi kuphunzira Mau a Mulungu. Mabvuto a tsiku ndi tsiku anagonjetsedwa pogwiritsa nchito Buku Lopatulika lace ndipotsatira malangizo omwe analembedwa mkati mwace. Ndipo nthawi zonse, anauza Veronika, kuti anali kufunitsitsa kulankhula kwa Mulungu m'mapemphero atsiku ndi tsiku.

Pamene Veronika anacoka anali wothokoza cifukwa cokhala ndi bwenzi monga Elizabeti ndipo anadziwa kuti nayenso anayenera kukula poyanjana ndi Mulungu. Cimeneci anakacita pomapita ku chalichi mokhulupirika koposa, pophunzira mau a Mulungu ndi kupemphera kwa Mulungu tsiku ndi tsiku.

KUTSILIZA:

(Mtsogoleri) - Akristu onse ayenera kugwiritsa nchito njira yomwe Elizabeti anacitira kuti akule mu cisomo ca Mulungu. Pamene Kristu akhala mwa inu, muyenera kukhala ndi ciyanjano ca tsiku ndi tsiku ndi iye. Iye ndi bwenzi lathu ndipo adzatithandiza nthawi ili yonse tikamupempha. Koma poyamba tiyenera kuika mtima wofunitsitsa ndipo iye adzapereka mphamvu. Pamene muli kupembedza m'nyumba ya Mulungu, mumalandila mphamvu zokhalira tsiku ndi tsiku. Pamene mulikuwerenga mau ace tsiku ndi tsiku ndi kulankhulana naye, mumadzazidwa ndi cimwemwe ndi mtendere.

Pemphero:

Kuti mai aliyense opezeka aone cosoweka cake ca thandizo la Mulungu ndi kugwiritsa nchito mwai uli onse kuti adziyanjana ndi Kristu.



Mariya anatenga anansi ena a Lidiya kupita kukacezera Lidiya. Posacedwa azimai anayamba kucezera wina ndi mnzace. Mariya anapempha mwamuna wace kuti apite naye kukazecera Lidiya ndi mwamuna wace kukawaitana kuti akapembedze nawo ku chalichi. Posacedwa Lidiya anali ndi abwenzi ambiri atsopano. Koma Mariya sanaiwale Lidiya. Iye anapitiriza kumucezera ndi kumulimbikitsa.

## GAWO 4: MCHERE WA DZIKO

Pamene muli kupita ku msika, kukatunga madzi kapena kugwira nchito ku munda mukhoza kucitira umboni. Nthawi zambiri timaima ndi kulankhulana ndi abwenzi kapena anansi pa njira. Kodi timalemekeza Mulungu kapena kudandaula cifukwa ca nchito ndi mabvuto. Nthawi zambiri pamene tisekerera kapena kuimba nyimbo pakati pa mseu anthu ena amakhala osangalala pamene aona cimwemwe cathu. Cimwemwe ndi copatsirana.

Pamene tiri kupita minda kukadzala mbeu ya cifundo ndi cikondi ca Yesu Kristu pakati pa njira. Yesu adatiuza ife kukhala mchere wa dziko. Anthu onse osowa "mchere" pang'ono ife tikhoza kukhala "mchere" wa uthenga kwa anthu kufikira titazindikira kuti pali kanthu kena komwe tiri nako komwe ali kukasowa. Tikatero tikhoza kugawana nao za cikondi ndi cipulumutso ca Yesu Kristu.

Pemphero:

Pempherani kuti aliyense wa inu akhale mboni ya mphamvu ya kwa iye Sabata ino.

mau a Mulungu ndi kukhala wacifundo ndi waci-thandizo kwa anthu omwe ali pafupi nanu.

Ukhondo ndi magwiritsidwe nchito a ndalama ndi njira zocitira umboni, pakuti zimacinjirira kulongolora, ndikusakondwa ndi matenda.

GAWO 3:

Pali njira zambiri zogawira mbiri ya bwino. Anthu onse amafuma cikondi ndi kukoma mtima. Anthu amafuna kuona zotsatira za Uthenga Wabwino, osati kungobva. Cifukwa ca cimeneci citsanzo ca moyo ndi cabwino koposa ulaliki, ngakhale kuphunzitsa kupyolera mu ulaliki ndikofunikanso.

Lidiya anabwera kucokera kumudzi kudzalowa mu mzinda komwe mwamuna wace anapeza nchito. Iye sanadziwe aliyense mu mzinda. Iye sanali kulankhula cilankhulo ca mu mzinda. Mwamuna wace anapita ku nchito tsiku lonse ndi kupita ndi abwenzi ace usiku. Mai ameneyo anali wosikidwa ndi kubvutika. Tsiku lina anakumana ndi Mariya mu sitolo. Mariya, amene anali Mkristu, anali ndi nkhawa pa anasi ace. Iye adakhoza kuzindikira pongoona nkhope ya mai wacitsikanayo, kuti kanthu kena kanali kolakwika. Iye anamufunsa za banja lace, komwe anali kukhala, wakhala mu mzindamo kwa nthawi yaitali cotani. Lidiya anali wokondwa kulankhula. Mariya anaitanira Lidiya kunyumba kwace kukamwa tii, komwe adazolowelana. Mariya anamvetsera mabvuto a Lidiya. Ena anadzipereka kuti amuphunzitse cilankhulo ca mu mzinda ndi kudziwitsa kwa abale ace ena za iye. Iye anaitana Lidiya kuti apite naye ku chalichi ndi ku misonkhano ya W.M.U. potsiliza,



MUTU 3:

MUTU WA PHUNZIRO: MKAZI WATSOPANO

MUTU WA LERO: Mkazi Watsopano Kunyumba

MAU APAMTIMA: "Cifukwa cace monga momwe munalandira Kristu Yesu Ambuye, muyende mwa Iye, ozika mizu ndi omangirika mwa Iye, ndi okhazikika m'cikhulupiriro, monga munaphunzitsidwa, ndi kucurukitsa ciyamiko."
Akolose 2:6-7

KUFOTOKOZERA:

(Mtsogoleri) - Pa nthawi ino muyenera kudziwa bwino Elizabeti ndi Veronika. Lero tiona momwe amacitira njira zacikristu kunyumba. Pamene tidziwa zambiri za Kristu, tidzafuna kuti iye atitsogolere mu macitidwe athu onse. Timayenera kuyenda mwa Kristu pa mphindi ili yonse ya tsiku. Pamene tilephera kucita izi ndikusalankhula naye tsiku ndi tsiku, timaiwala nthawi zonse kukhala monga iye. Pamene tiri kumva za azimai awiriwa lero, onetsetsani ngati inu muli ofanana ndi m'modzi wa iwo.

GAWO 1:

Pamene Veronika anali kutsiliza nchito ya pa tsiku ya m'munda anali kuganizira mau amene Mbusa Petro ananena pa sande ku chalichi. Iye ananena kuti mai aliyense ayenera kuphunzitsa ana ace njira ya Mulungu. Posacedwa anafuna kuona kuti ana ace onse anali kupita ku chalichi ndi iye. Nthawi zina ana awiri akuru anali kupita, koma anali kutopa nthawi zonse motero kuti sanali kusauka ndikutenga ocepera.

Poonjezera anaganiza kuti akanakhoza kuphunzira za Yesu pamene ali akuru.

Iye anapita mkati nayamba kukakonza cakudya ca banja lace. Pamene akuru akuru anafika kucokera ku Sukulu ndipo pamene mwamuna wace anafika kucokera ku nchito akanakhala ndi njala onse. Iye analibe nthawi yodalitsa cakudya koma kuyamba kuwagawira atangofika. Usiku umenewo onse atagona, anaganizira pamene anali kutseka maso ace, "mawa ndidzayesa kuwauza za Yesu ndikuwaphunzitsa njira za Mulungu."

GAWO 2:

Elizabeti naye, anali ndi nchito yambiri yoicita tsiku ndi tsiku. Poonjezera kusamarira banja lace lalikuru, mai wace odwala amene anali kukhala naye. Kawiri kawiri panali anansi amene anali kukhala nao. Pamene mwana wace anali kudzuka m'mawa uli wonse, anali kumumva ali kuimba nyimbo yatsopano imene anaiphunzira ku chalichi. Tsiku lina pamene anali kuimba, anadabwa pamene mwana wace wa zaka zisanu anayamba kuimba nayenso. Kawiri kawiri anali kuimba pamene anali kugwira nchito kunyumba kapena m'munda.

Iye anayesa kwambiri kutsatira malangizo a mbusa wace. Iye anadziwa kuti ayenera kuphunzitsa onse ana ace Mau a Mulungu motero kuti akonde Yesu monga momwe anamukondera iye. Nthawi zambiri anali kuwauza zinthu zimene iye anaziphunzira mu kalasi yaubatizo. Ndipo pa sabata ili yonse anali kuthandiza kuti onse amvetsetse ndi kukonzekera sande sukulu. Iwo akanakhoza kuphunzira zambiri kucokera ku



Kuyambira pa nthawi ya m'mawa lolani kumvetsetsa ndi cimwemwe ndi mphamvu zipitirizike kuti zindizendeze pafupi ndi inu ola liri lonse la tsiku."

Kodi inu mumayamba tsiku lanu motani? Ngati tipemphera kwa Mulungu asanadzuke pa bedi m'mawa, cimeneci cidzathandiza kutikonza pa kupembedza Mulungu kupyolera tsiku lonse lathunthu.

Kuwerenga ndime za Buku Lopatulika monga Masalmo 5, 8, 11, 19, 23, 25, 46, 62, 90; 1 Yohane 3; 1 Akorinto 13 ndikupempherera pamodzi ndi banja m'mamawa kumatithandiza kukhala oyanjana ndi Mulungu ndi wina ndi mnzace.

GAWO 2: NCHITO YANU

Popeza nchito ndiyopatulika, tiyenera kukonzeratu bwino kuti ikhale yokondweretsa Mulungu. Pamene muli kutsuka mbale ndi madzi otentha ndi sopo, kodi mumadziwa kuti imeneyi ndi njira yocitira umboni? Cifukwa pamene muli kutsuka mbale mosamala, mukhoza kuteteza banja lanu kuti lisadwale, ndipo mukhoza kupereka mphamvu yopembedzera ndikucitira umboni za Mulungu. Pamene muli kusesa mnyumba yanu mukhoza kupemphera kuti Mulungu asese mu mtima mwanu kuti muyere tsiku ndi tsiku. Pamene muli kucapa zobvala ndi kucisa, mukhoza kupemphera kuti Mulungu adzathandiza mzimu wa Akristu kuti akhale ozindikira ndikukhala abwino monga maonekedwe akunja kwa zobvala.

Muyenera kukonzeratu nchito yanu kotero kuti mukhale ndi nthawi yosewela ndi kuphunzitsa ana anu, kulankhula ndi mwamuna wanu, kuphunzira

PHUNZIRO 9

MUTU WA PHUNZIRO: UMBONI WA MACITIDWE ATSIKU NDI TSIKU

MUTU WA LERO: Macitidwe Atsiku ndi Tsiku A Kunyumba ndi Mu Mzinda

MAU APAMTIMA: "Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwako kwafika, ndi ulemerero wa Yehova wakuturukira."
Yesaya 60:1

KUFOTOKOZERA:

Moyo uli ndi zocitika zambiri zocitika tsiku ndi tsiku. Zimenezi mwa izo zokha zingaoneke ngati zopanda nchito, koma poziika pamodzi zimapanga moyo kuti udziyenda bwino ndi kutipatsa ife cimwemwe. Nthawi zambiri timatopa pa nchito ya tsiku liri lonse, koma pamene tilingirira kuti Mulungu adatipatsa nchito, ndipo nchito ndi yoyera kwa iye, kodi ticita ciani, timagwirira iye.

Ngati Mulungu anakudalitsani ndi nyumba ndi banja. Umenewu ndi umboni wa tsiku ndi tsiku. Kodi nanga, mungakhale ndi cikondi motani, kudekha, kumvetsetsa ndi mphamvu kukhala mboni m'macitidwe atsiku ndi tsiku?

GAWO 1: YAMBANI TSIKU LANU NDI MULUNGU

"Tsiku la lero, Ambuye, thandizeni kukupembedzani, thandizeni kuti ndidzazidwe ndi cimwemwe ca tsiku la tsopano, mwai watsopano. Patseni nzeru za mu nchito ya lero. Thandizeni kuti ndikhale wofatsa, wokonda ndi wosasiliza.



maphunziro ao. Iye anayesetsa kukhala okondwa kwambiri ndi kumvetsetsana ndi aliyense wa ana ace.

GAWO 3:

Atangokhala Mkristu, Elizabeti analankhulana ndi mwamuna wace. Iye anafotokoza mwapafupi monga anathera kuti Yesu analowa mu mtima mwace ndipo ayenera kucita monga Mau a Mulungu amanenera. Iye anamufunsa kuti adzapite ku chalichi ndi iye ndi kupemphera mu mtima kuti nayenso, akanakhala Mkristu. Yohani sanali wokondweretsedwa kuti apite ku chalichi kapena kukhala Mkristu, koma iye anaona mwamsanga kusintha kwa ana ace. Motero iye anakhala wofatsa kumvera pempho lace.

Imodzi ya nthawi yosinthika koposa inali ya cakudya. Siunali mwambo kuti banja linali kudyera pamodzi, koma Elizabeti adayesetsa kuti zidzitheka. Ndipo anali kuyamba cakudya ndi mau a pemphero kuthokoza kwa Mulungu cifukwa ca cakudya ali naco. Posacedwa mwamuna wace anayamba kuwelama mutu ndi mkazi wace pamene anali kutsogolera dalitso. Iye anayamba kukhala osiyana mkati. Ndipo tsiku limodzi la sabata; pamene Elizabeti anamupempha kuti apite naye (anali kumamupempha kawiri kawiri), iye anapita. Cimwemwe cinadzala mtima mwace ndipo anamvetsetsa cifukwa cimene Mkristu ayenera kukhala monga Kristu kunyumba.

GAWO 4:

Pali njira zambiri zimene tingaonetsere cikondi ca Mulungu pamene tiri kuyenda-yenda ndi kucita nchito ya tsiku ndi tsiku m'nyumba

zathu ndi kumunda. Cinthu cimodzi cimene tiyenera kucisunga m'maganizo athu nthawi zonse ndico "kuyenda mwa Kristu." Imeneyi sinchito yapafupi, ndipo tiyenera kumapemphera nthawi zonse kuti Mulungu adzatitsogolera ndi kutipatsa mphamvu ndi cilimbitso kucitira zimenezi.

Tangoona pang'ono njira yocepa yomwe Elizabeti ndi Veronika adaisankhula kuitsata. Kodi mwaona kuti Veronika anasankha njira yapafupi? Timakonda kunena zimenezi ponena kuti mawa ndidzayamba. Koma kawiri kawiri mawa silifika. Sitingasiye udindo wa cikristu cathu. Ana athu ayenera kuphunzira tsopano, asanakhale anthu akuru ndi kuphunzira njira zina zomwe siziri za Cikristu. Ngakhale mwana wa mng'ono akhoza kuyamba kumva za cikondi ca mpulumutsi wathu. Elizabeti anali wokhulupirika kuthandiza banja lace kuti amvetsetse njira za Kristu. Nthawi zonse anali kucita monga anamvera Mulungu akumuuza kuti acite. Iye anagawira cikhulupiriro cace ndi mwamuna ndi ana ace.

KUSILIZA:

Azimai onse ali ndi nchito yosamalira nyumba zao ndi mabanja, koma akhoza kucita zinthu zimenezi mu njira zambiri kuonetsa cikondi ca Mulungu. Ngati iwo asiya cifukwa cotopa ndikusiya kuthandiza mabanja ao kuti amvetsetse njira ya Mulungu, idzakhala njira yobvuta kwambiri. Koma ngati tiyamba tsiku liri lonse ndi thandizo la Mulungu, tikhoza kugwiritsa nchito mwai uli onse kuonetsa okondedwa athu za Yesu ndi cikondi cace. Kodi mumayesa tsiku liri lonse kugawira cikhulupiriro canu ndi banja lanu? Pamene tiri kupemphera, tiyeni tipemphe Mulungu kuti atipatse mphamvu.



piriro. Tsiku lina mfumu ya m'mudzimo idabwera. Iye anakondweretsedwa kotero kuti naye anafuna kukhala Mkristu. Motero anabwerera kunyumba kwace nakatenga cuma cace capadera. Adapereka mkondo wace, uta ndi mpaliro ndi zinthu zina zofunika. "Tengani izi ine ndifuna kukhala Mkristu." Wacimishoni anamufotokozera kuti poyamba Mulungu afuna iye, ndipo akhoza kupulumutsidwa. Mosamvetsetsa mfumu idati, "Inde, ndine wa nzeru ndi mtsogoleri. Ndidzasonkhanitsa anthu anga tsiku ndi tsiku ndikuwaphunzitsa kucokera mu Buku la Mulungu. Ndipo ndidzakhala Mkristu." Kaciwirinso, adamuuza kuti Mulungu yekha ndiye adamufuna kuti akhulupirire mwa Yesu ndipo akhoza kupulumutsidwa. Mfumu idacoka mokhumudwa.

Sabata lina pamene wacimisoni adafika, mfumuyo inali yoyamba pamalopo. Iye anati, "Sabata lonse ndakhala ndiri kufunsa kumvetsetsa. Tsopano ndadziwa kuti ndiyenera poyamba kudzipereka ndekha kwa Yesu. Ndipo ndikhoza kupereka zomwe ndiri nazo ndikukhala ndi mtendere mu mtima."

Mfumu inaphunzira phunziro tonsefe tiyenera kuphunzira. Tiyenera kuphunzira kudzipereka tokha.

Pemphero:

Khalani ndi mau apemphero kupempherera aliyense wopezeka kuti afufuze mtima wace ndi kuti aone ngati anaperekadi zonse kwa Yesu. Tsekani ndi nyimbo, "ndipereka zanga zonse kwa Yesu."

Mulungu ndi banja lace ndi abwenzi. Kupyolera mwa cikondi cace ca pa ena anakhoza kukhala mtumiki wa nchito ya Mulungu. Cikondi cinamupatsa mphamvu yocitira umboni m'dzina la Kristu. Ngakhale Samueli monga munthu anali wofooka, cikondi cace cinamulimbikitsa.

GAWO 3: DZIPEREKENI WATHUNTHU

Pamene Mkristu adzipereka yekha ndi cikondi cace, adzafuna kupereka zonse zimene alinazo. Mulungu samatifunsa kucita koposa zomwe sitingathe. Popereka zathu zonse tiyenera kugwiritsa nchito matupi athu monga okhulupirira Mulungu. Mu Aroma 12:1 limanena kuti, "perekani matupi anu nsembe ya moyo, yopatulika, ndi yobvomerezeka kwa Mulungu." Tiyenera kusamala matupi athu. Thupi lanu ndi kacisi wa Mulungu.

Cuma cathu cikhoza kuperekedwa kuti Mulungu acigwiritse nchito. Tidzazidwa kwambiri ndi Mzimu wa kupyolera mwakuzipereka tokha; cikondi cathu, matupi ndi nzeru zathu, kudzipereka kwinako kudzatsatira. Mulungu amangofunsa za cakhumi, koma adzafuna kuti tidzipereka zopereka poonjezera zimenezi.

KUMARIZA:

(Mtsogoleri) - Tiyeni titseke maphunziro athu lero ndi nthano iyi. Mwina mwace idzatithandiza kuti timvetsetse udindo wodzipereka tokha kwa moyo. Panali mudzi wina waung'ono pafupi ndi mpingo wa Baptist. Sabata iliyonse sing'anga ndi mlaliki anali kupita kumudzi umenewu kukauza anthu a m'mudzi za Kristu ndi kukawaciritsa. Ambiri anadzipereka mwacikhulu-



Pempherani:

Kuti mkazi ndi mai aliyense adzatenga Kristu kupita naye kunyumba ndipo adzagawira cikondi cace ndi ena onse.

PHUNZIRO 4

MUTU WAPHUNZIRO: MAI WATSOPANO

MUTU WA LERO: Mai Watsopano Pakati Pa Anthu Ndi Mpingo

MAU APAMTIMA: "Koma tisaleme pakucita zabwino pakuti pa nyengo yace tidzatuta tikapanda kufoka."
Agalatiya 6:9

KUFOTOKOZERA:

Pamene tiri kupitiriza kukula mu cisomo ca Mulungu ndi ubwino, timazindikira za maudindo ena ambiri mu midzi yathu, pakati pa anthu ndi mu mpingo. Timayenera kukhala ndi nkhawa ya kwa onse tikumana nao tsiku ndi tsiku. Pamene tiwerenga m'malembo, tisamaleme pocita zabwino. Ndife mboni tsiku ndi tsiku kwa abwenzi ndi onse amene oyandikana nafe. Kodi ife tiri kudalira umboni wotani pamacitidwe athu ndi kukhulupirika kwathu kwa Mulungu.

GAWO 1:

Elizabeti ali ndi nkhawa ya pa abwenzi ace. Kawiri kawiri azimai amakonda kuceza madzulo.

Nthawi zambiri kunali nkhani zina, koma popeza Elizabeti anakhala Mkristu, nthawi zambiri anali kulankhula za Yesu ndi zinthu zomwe anaziphunzira ku chalichi. Azimai owerengeka anali a cisilamu; ena analibe cipembedzo ciri conse. Tsiku lina la W.M.U. ndi pa sabata anali kuitana abwenzi ace kudzaceza naye. Nthawi zina anali kupita kukakhala nao pa msonkhano. Iye adadziwa kuti unali udindo wace kukaceza ndi colinga, colinga couza ena za Yesu.

Veronika anali kuphunziranso. Cinali cobvuta kwa iye kuuza ena za Yesu. Nthawi zina abwenzi ace anali kuseka pamene anali kuwauza kuti apita ku chalichi. Ngati anali kukhala ndi nthawi yabwino yoceza sanali kupitako, koma mu mtima mwace anadziwa kuti kutereku ndikulakwa ndipo cinali kumubvuta.

GAWO 2:

Pamene masabata anali kupita Elizabeti anali kuphunzira njira zina zomwe iye akaonetsera ena cikondi ca Mulungu. Iye anali ciwalo ca mpingo ca nchito ya W.M.U. Ndipo kupyolera mu mbali ya dela lace anakhoza kutumikira ndi kucitira ena zambiri. Pamene abwenzi ena omwe sanali acikristu akakhala ndi ana, anali kupeza kuti inali nthawi yabwino kukawacezera ndikukawapatsa timabuku ting'ono-ting'ono ndi dongosolo la cipulumutso mkati mwace ndi ndime za mu Buku Lopatulika.

Mwai wina wocitira umboni unabwera pamene mu mudzimo munali maliro. Unali mwambo wa anthu onse a m'mudzimo kupita kunyumba ya maliro ndi kukalira nao ku masiku owerengeka. Elizabeti anadziwa kuti imeneyi sindiyo njira



mpingo wa Baptist. Onsewo anali Akristu abwino. Iwo sanali ndi ndalama imodzi yomwe kapena katundu wa iwo eni. Kunena zoona anali ndi mabvuto a akuru pofuna kulipirira ndalama za sukulu yao. Koma iwo anafuna kutumikira Mulungu, ndipo anaganizira kuti zomwe akanacita akanazipereka eni okha. Cimeneci cinatanthauza nthawi ina ya nchito ya padera. Iwo anali kuphunzitsa ku chalichi, anali kuthandiza azimai pa nthawi yopembedza ndi ana ocepa, anali kuthandiza abusa ao ndi maudindo ena ambiri. Tsiku lina anaganizira kuti anafuna kukhala ogwira nchito ya Cikristu ku nthawi zonse atatsiriza sukulu yao. Mbusa anali wokondwera kwambiri, koma iye anawauza kuti, "inutu ndinu ogwira nchito kale nthawi zonse, cifukwa munapatsa Mulungu cintu cofunika koposa, inu eni."

GAWO 2: KUPEREKA CIKONDI CANU

Kodi cikondi ndi ciani? Mulungu ndiye cikondi, ndipo iye anakukondani koposa kotero kuti anapatsa Yesu kuti inu ndi ine tikhale nao moyo wosatha. Pamene munabvomereza Kristu, mudafika ndi cikondi mu mtima mwanu. Cikondi cimeneci cinali capafupi, monga cikondi ca mwana ca pa makolo ace. Pamene tinakhala Akristu olimba, tinayamba kuzindikira mphamvu ya cikondi cimeneci.

Samueli anali wa zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu pamene anakhala Mkristu. Ku nthawi yace yoyamba m'moyo wace wonse, anadzazidwa ndi cikondi, cikondi ca Mulungu. Pamene anali kukula m'cidziwitso ca Mulungu ndi Kristu, cikondi cace cinaonjezekera. Iye anagwira nchito kwambiri kugawira ena cikondi cace ca

PHUNZIRO 8

MUTU WA PHUNZIRO: KUDZAMA MUUZIMU

MUTU WA LERO: KUPYOLERA MUKUDZIPEREKA KWA WEKHA

MAU APAMTIMA: "Ndipo si monga tidayembekeza; koma anayamba kudzipereka okha kwa Ambuye, ndi kwa ife mwa cifuniro ca Mulungu."
2 Akorinto 8:5

KUFOTOKOZERA:

Kwa masabata atatu apitawa takhala tiri kuphunzira momwe tingakhalire Akristu abwino kupyolera mu kukhulupirika kwathu mu kabweredwe ka ku chalichi, kupyolera mu makhalidwe abwino a mapemphero, ndi kupyolera mukuphunzira mau a Mulungu. Pamene ticitadi zinthu zimenezi tidzafuna kudzipereka athunthu kwa Kristu. Cikristu coonekera ndi cipembedzo copereka. Mulungu anapatsa munthu moyo. Iye anapereka mphatso yaikuru ya Mwana wace Yesu. Ifenso pobwereza tifunsidwa kuti tipereke. Kodi tikhoza kupereka ciani?

GAWO 1:

Cimeneci ndi cinthu cobvuta kucicita. Kawiri kawiri ndi kwapafupi kupereka zinthu koposa kudzipereka iwe mwini. Mu 2 Akorinto 12:14 tiwerenga "pakuti sindifuna zanu, koma inu." Motero musanayambe kudandaula popereka zomwe tiri nazo zinthu zomwe tiri nazo, tiyenera kukhala ofunitsitsa kupereka zofuna zathu ndi zolakalaka zonse za Mulungu.

Mu mudzi wina munali atsikana awiri mu



ya Cikristu. Iye anali kugwira nchito mnyumba kukonza zakudya za anansi onse kapena kuthandiza monga angathere. Pamene anali ndi mwai wotonthoza abwenzi ace, anali kuwerenga kucokera mu Buku Lopatulika lace ndikufotokoza kuti Mulungu ndi Mulungu wa cikondi ndipo awapatsa mphamvu ngati atangopempha iye. Nthawi zina abwenzi ace anali kumupempha kuti apempherere iwo kwa Mulungu.

GAWO 3:

Tsopano popeza anali ziwalo za mpingo wa Baptist kwa kanthawi, panali zinthu zambiri za Veronika ndi Elizabeti zocita. Elizabeti anapemphedwa kuphunzitsa sande sukulu ya ana pamene aphunzitsi ao apita kukacezera anansi. Iye anali asanaphunzitse kale lonse, koma potsiliza anaganizira kuti ayesetsa kucita bwino.

Pamene mpingo unakonza maphunziro amasiku atatu a atsogoleri a mipingo a mu association, Veronika ndi Elizabeti onse anadzipereka kuthandiza kuphika cakudya tsiku liri lonse. Ngakhale adacita nchito ina yoonjezera, iwo anali okondwa kukhala ndi mbali mu nchito ya Mulungu.

Mu W.M.U. azimai anali ndi mwai woposa kutenga mbali ya pologalamu. Pamene nthawi yafika yokambirana za mabvuto ndi zobvuta, anali kutenga mbari, osaopa kunena momwe anali kuganizira. Mwezi ulionse anali kupita ndi magulu ena pakati pa anthu kukayendera odwala kapena anthu amene sanabwere ku mapemphero kwa nthawi yaitali.

GAWO 4:

Potseka phunziro lathu la mkazi watsopano tiyeni tiyang'ane ku ndime zimene taziphunzira. Tsiku loyamba 2 Akorinto 5:17. (ndipo uzani ena anene kuti cimeneci citi ciani kwa iwo?. Kodi inu munakhala munthu watsopano mwa Kristu? ngati munakhala, kodi mudayesa kutaya zinthu zakale m'moyo wanu zomwe zinali zolakwika?

Tsopano werengani 1 Petro 2:1-3 kapena ineneni pa mtima ngati mwaiphunzira. (Khalani ndi wina okonzekera kuwerenga). Kodi mukufunadi kumva mau a Mulungu ndikuphunzira kucokera kwa iwo? Ngati mukufuna, mudzakhala okhulupirika pobwera ku chalichi kudzapembedza iye. Mudziwerenga Buku Lopatulika lanu, kapena khalani ndi wina wace kuti akuwerengeleni tsiku ndi tsiku kuti mukule mu cisomo ca Mulungu.

Tsopano tembenukirani mu Akolose 2:6-7 ndipo tiwerengera pamodzi limeneli. Kodi mumayenda mu mapazi Akristu? Kodi inu ndinu ozama mwa Iye? Muyenera kutsata ziphunzito zace mu zinthu zonse zomwe mucita ndi zomwe muli. Kodi nyumba yanu ionetsa kuti mukonda Mulungu?

Potsiriza, tiyeni tiwerenge ndime yathu ya lero, Agaltiya 6:,9-10. Ngati tatsata mau a Mulungu ndi kucita zinthu zinazi kukula mu cikondi cace, sitidzalema kucitira ena. Tidzagwiritsa nchito mwai ulionse kuthandiza abwenzi athu ndipo adzaona mai watsopano.

Pemphero:

Pemphani aliyense wopezeka kuwerama mutu



Posacedwapa anali ndi njira ina yophunzirira Buku Lopatulika lace. Mbusa wace anali kuphunzitsa buku la Yakobo. Iya anafunsa aliyense kuti akawerenge bukuli pakati pa sabata. Motero adaphunzira buku limodzi sabata yonse. Iye anakonda bukuli ndi sabata yamawa anayamba kuphunzira buku lina. Kawiri kawiri anali kuloweza ndime zapadera zimene zikanathandiza kucitira umboni bwino.

KUMALIZA:

Tsopano, tiyeni tiona njira zokhalira wophunzira wa bwino wa mau a Mulungu. Tizirembe kuti nonsenu muzione. (Ziwerengeni ndi kuziremba pa bolodi kapena pa cipepala cikulu. Lankhulani pa njira ili yonse pamene muli kuziwerenga).

1. Werengani Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku.

2. Kupeza nthawi yabwino ndi malo wophunzirira tsiku ndi tsiku.

3. Kutsata dongosolo la kawerengedwe.

   Werengani Buku Lopatulika kungopyolamo.

   Tsatani kalendara yowerenga Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku. Phunzirani ndime zomwe zitsata phunziro la Sande Sukulu.

   Phunzirani Buku limodzi panthawi imodzi.

Ngati mutatsatira malingaliro opatsidwawa mudzapeza cithandizo cacikuru kucokera pophunzira Mau a Mulungu. Posacedwa mudzapeza njira zakaphunziridwe katsopano ndikugwiritsa nchito Buku lace, Buku Lopatulika.

ngira ndalama zogulira Buku Lopatulika.

M'mawa uliwonse mwamuna wace atapita ku nchito ndi ana atapita ku sukulu, anali kutenga kabuku kace kakang'ono ka Yohane ndikuwerenga. Iye anali kumawerenga ndime zowerengeka tsiku ndi tsiku, kawiri kawiri anali kuwerenga mobwereza kawiri kapena katatu. Nthawi zina anali kukonda kuwerenga kotero kuti sanali kusiya ndipo anali kuwerenga ndime imodzi kapena ziwiri. Linali lodzazidwa ndi mau odabwitsa omuuza za Yesu ndi kumuthandiza kuti akhale Mkristu wa mphamvu. M'masiku ena anali kumawerenga ndime zomwe anawerenga kale. M'njira imeneyi anakhoza kuphunzira Buku Lopatulika lace tsiku ndi tsiku.

## GAWO 3:

Beti anali wapampando wa W.M.U. ndi Mkristu wodzipereka. Iye anali kuwerenga Buku Lopatulika lace tsiku ndi tsiku kwa zaka zambiri. Cinthu cofunika kukumbukira koposa za kuphunzira Buku Lopatulika, iye anati, cinali kudzipatulila nthawi ndi malo owerengera ndi kuphunzira.

Pamene anayamba kuphunzira Buku Lopatulika lace tsiku ndi tsiku, anaganizira kuyamba ndi Genesis ndi kuwerenga Buku Lopatulika lonse. Anacita zimenezi kawiri, nthawi zonse anapezamo maganizo atsopano omuthandiza. Ndipo anaganizira kuti atsate kalendara powerenga Buku Lop ulika tsiku ndi tsiku kwa caka cimodzi. Iye anacita ici mokhulupirika. Nthawi zina anali kuwerenga ndime sabata iliyonse imene inali kuphunzitsa za sande sukulu.



wace. Khalani ndi pemphero lalifupi kucokera kwa aliyense amene afuna kupempha thandizo la Mulungu pamene alikuyenda m'mapazi ace ndikukhala moyo wokondweretsa Kristu tsiku ndi tsiku.

## PHUNZIRO 5

MUTU WA PHUNZIRO: KUZAMA MWAUZIMU

MUTU WA LERO: Kupyolera mu Kupezeka ku Chalichi

MAU APAMTIMA: "Tumikirani Yehova ndi cikondwerero: Idzani pamaso pace ndi kumuyimbira mokondwera."
Masalmo 100:2

MTSOGOLERI:

Kwa miyezi iwiriyi tikhala tikuphunzira njira zomwe tingakhalire wofanana ndi Kristu. Pali njira zina zabwino zomwe tingakhalire akuya mu mzimu. Palibe iliyonse yapafupi ndi yosabvuta, koma zonsezi zimafuna kuti ife tigwire nchito tsiku ndi tsiku. Zimenezi ndi kukhala okhulupirika kupezeka ku chalichi, pemphero la tsiku ndi tsiku, kuphunzira Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku, kupitiriza kudzipereka wekha, ndi umboni wa Cikristu. Ndikupyolera mu mphamvu ya Mulungu ndi thandizo kuti ife tikhoza kukhala ndi makhalidwe a Kristu.

Lero tiona mayankho amafunso ena ofunsidwa ndi Akristu ena amene afuna kukula mu

**cikondi ca Mulungu. Kodi ndi cifukwa ciani kupita ku chalichi kuli kofunika kwambiri?**

**GAWO 1:**

**Ambiri a ife timapita ku chalichi kawiri kawiri. Tiyeni tiyambe ndi kufunsa funso. Kodi inu mumabwera ku chalichi cifukwa ciani, kapena ku misonkhano ya W.M.U.? (Dikirani mai wina kuti ayankhe). Ngati palibe wina wanena kanthu, chulani wina kuti anene cifukwa cimene iye amabwerera.) Ndiganiza kuti tonsefe tibvomerezana kuti timabwera ku chalichi kudzapembedza Mulungu ndi kudzalandira mphamvu za kakhalidwe ka tsiku ndi tsiku.**

**Mpingo ndi gulu la anthu okhulupirira obatizidwa. Sitiyenera kukhala ndi nyumba ya chalichi kuti tikhale ndi mpingo. Mwina mwace ena a inu mwakhala ku machalichi a mu nyumba kapena panja poyera. Chalichi ndi malo a anthu a Mulungu kumupembedza iye pamodzi. Mulungu amadziwa kuti tiyenera kukhala pamodzi kugawana cikondi cathu ca kwa iye. Pobwera ku chalichi tikhoza kuyanjana ndi Akristu ena. Pamene ife ticita zimenezi, mitima yathu imadzazidwa ndi kupezeka ndi mphamvu yace. Pamene ife tikhala wodzazidwa ndi mphamvu ya Mulungu timakhala ozindikira udindo wathu pomutumikira iye. Chalichi ndi malo opembedza.**

**GAWO 2:**

**Cifukwa cina comwe tiyenera kupitira ku chalichi pa nthawi yonse ndi kukamva mau a Mulungu. Tiri ndi mwai kukhala ndi atsogoleri abwino mu mipingo yathu amene atsogozedwa ndi Mulungu. Pa tsiku la sabata liri lonse m'mawa**



kukumbuka zonse zimene ziri kulankhulidwa. Koma kodi iye akadamawerenga Buku Lopatulika lace motani tsiku ndi tsiku ngati iye sanali kuwerenga?

Iye anapeza mayankho awiri kubvuto lace. Coyamba anapempha m'dzukulu wace amene anali kuphunzira sukulu kumabwera kunyumba kwace tsiku ndi tsiku kudzamuwerengera. Onsewo anali kuyang'anira nthawi imeneyi. Pamene masabata anapitapo ndikuti anali kutha kumamva mau a Mulungu tsiku ndi tsiku anadzazidwa ndi Mzimu. Umboni wace unali wa tsiku ndi tsiku wa cikondi ca Mulungu. Ndi mwai womamva mau a Mulungu kawiri-kawiri, anazolowera ndime zina zomwe zinali ndi matanthauzo apadera a kwa iye. Anagwira nchito yaikuru yoloweza ndime zambiri. Kawiri-kawiri Buku Lopatulika anali kungonena ndime ndikuganizira za matanthauzo ace. Posacedwa Buku lace linali m'mutu m'maganizo ndipo anakhoza kuligwiritsa nchito nthawi iliyonse.

GAWO 2:

Sela Mwaponya anali Mkristu watsopano. Mwamuna wace ndi banja sianali Akristu ndipo cinali cobvuta kwambiri kwa iye kupita ku chalichi kawiri-kawiri. Koma anali kupita nthawi zonse zomwe anakhoza. Mbusa wace anamuuza kuti monga Mkristu ayenera kumawerenga mau a Mulungu tsiku ndi tsiku. Koma iye analibe Buku Lopatulika ndipo analibe ndalama zogulira bukulo. Kodi iye akanakhoza kuwerenga mau ace tsiku ndi tsiku motani ngati iye analibe Buku Lopatulika? Pamene adapita kwa mbusa wace kukamuuza za bvuto lace, anamupatsa kabuku kakang'ono ka Yohane kucokera mu Cipangano Catsopano. Iye anamuuza kuti ayambe kudzisu-

PHUNZIRO 7

MUTU WAPHUNZIRO: KUZAMA MUUZIMU

MUTU WA LERO: Kupyolera Kuphunzira Buku Lopatulika

MAU APAMTIMA: "Ucite cangu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomerezeka, wa nchito wopanda cifukwa ca kucita manyazi, wolunjika nao bwino mau a coonadi."
2 Timoteo 2:15

KUFOTOKOZERA:

(MTSOGOLERI) - Mkristu aliyense amene afuna kuphunzira zambiri za Mau a Mulungu ayenera kuganizira za njira yabwino yophunzirira Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku. Popeza tiri ndi maudinso osiyana-siyana kunyumba ndiponso popeza maziko a nthano zathu amasiyana, tikhala tiri kuona za azimai ena amene anapeza njira zopambana zophunzirira Mau a Mulungu tsiku ndi tsiku. Pamene muli kumvera za azimai amenewa, kodi mukhoza kupeza njira yatsopano imene idzakuthandizani "phunzirani kuti mudzionetsere nokha wobvomerezeka kwa Mulungu?" 2 Timoteo 2:15.

<u>GAWO 1</u>:

Amai Magret anali ndi ana ambiri ndipo onsewo anapita kusukulu. Iye anali wonyadira cifukwa ca iwo, kweni kweni popeza iye anali asanaphunzire kulemba ndi kuwerenga. Iye anali kukonda kupita ku chalichi ndikukamva mau a Mulungu akuwerengedwa. Iye nthawi zonse anali kumvetsera mosamala bwino kotero kuti akhoze



aphunzitsi athu a sande sukulu ali ndi phunziro la Buku Lopatulika. Iwo amakhala atagwira nchito ndi kuphunzira kwambiri kudzaphunzitsa ife zambiri za mau a Mulungu. Mu W.M.U. tiri ndi dongosolo la maphunziro abwino otiphunzitsa ife. Koma pofuna kulandira ziphunzitso zimenezi, tiyenera kumabwera, kumvetsera ndi kutenga zomwe tazimva kuti zikhale mu mitima yathu.

Abusa athu ndi anthu osankhidwa ndi Mulungu amene amalankhula kwa ife kupyolera mu mphamvu yace. Ngati ife titamvera ndi kutsatira ziphunzitso zao, tidzakula mu cisomo ca Mulungu tsiku ndi tsiku. Kupyolera mwa kukhulupirika kwathu kokha tikhoza kukondwa pomayenda ndi Mulungu tsiku ndi tsiku. <u>Ku chalichi kwathu ndi malo omvera mau a Mulungu.</u>

<u>GAWO 3</u>:

Timaphunzira njira zambiri kutsatira ziphunzitso za Kristu pomapita ku chalichi. Kupyolera mu msonkhano wa mapemphero athu timaphunzira momwe tingapempherere. Musonkhano wa mapemphero tikhoza kuona atsogoleri athu a Cikristu ali kupemphera. Tikhoza kuwatsatira pamene ali kutsogolera. Mu misonkhano yathu ya W.M.U. tikhoza kuphunzira kutenga mbari mu msonkhano. Pomatenga mbari mu msonkhano wa sabata ndi sabata, timakhala otsimikiza kuti Mulungu adzatithandiza mu ziri zonse tingacite. Mantha athu a polankhula za Kristu ndi potenga nchito zautsogoleri mu mpingo zidzacoka. <u>Ku Chalichi kwathu ndi malo ophunzira Mau a Mulungu, mapemphereredwe ndi kalengedwe ka mbari ya utumiki.</u>

GAWO 4:

Cifukwa cina cacikuru kwambiri copitira ku chalichi ndi cakuti tikhoza "kulowa zipata zace ndi mayamiko ndi mabwalo ace ndi cilemekezo." Pamene Kristu akhala woonadi m'miyoyo yathu, timakhala oyamikika mphatso zace zonse za kwa ife. Tiyenera kumapita ku nyumba yace, chalichi, kukayamika Mulungu ndi mau athu ndi mitima.

Kodi mudayamba mwapita ku chalichi ndi colinga cimodzi conena kuti "Zikomo, Mulungu" cifukwa ca moyo wosatha, cifukwa ca Yesu, cifukwa ca cakudya, cifukwa ca mvula, cifukwa ca banja, cifukwa ca nyumba ndi cikondi. Mulungu ndi wabwino. Iye ndi cikondi. Ku Chalichi kwathu ndi malo a ciyamiko ndi kothokozera.

KUMARIZA:

(Mtsogoleri) - Tsopano, tiyeni tichule zifukwa zina zomwe timapitira ku chalichi. (Tsogolerani gulu poyankha). Timapita ku chalichi kukapembedza pamodzi ndi abale mwa Kristu. Timapita kukamva mau a Mulungu kuti akhale mbali ya miyoyo yathu. Timapita kukaphunzira njira zabwino zokhalira Mkristu ndi kutumikira Mulungu. Potsiriza timapita kunyumba ya Mulungu kukaimba zoyamikira dzina lace ndikukaonetsa mayamiko athu cifukwa ca cikondi cace. Pocita zinthu zonsezi tidzayenda pafupi ndi Mulungu ndipo iye adzalamulira mokwanira bwino mu miyoyo yathu. Potsiriza phunziroli tiyeni tiwerenge pamodzi Masalmo 100.



GAWO 4: KODI AKRISTU AMAPEMPHERA BWANJI?

Mbusa Edward anali kuphunzitsa sukulu la za pemphero. Iye anawauza kuti pamene akupemphera ayenera kukhala ndi mtima woyera. Coyamba, aliyense ayenera kusiya maganizo a za dziko. Pamene cimeneci cacitika, maso ayenera kutsekedwa ndi mitu kuweramitsidwa. Nthawi zambiri munthu amagwada pansi asanayambe kulankhula kwa Mulungu.

Timauzidwa mu mabuku athu Opatulika kupemphera mwa cikhulupiriro; osakaika. Kawiri kawiri timapereka mapemphero athu kwa Mulungu ndi cikhulupiriro cocepa, ndipo kawiri kawiri timakaika kuti adzayankhidwa. Koma pamene tikula m'moyo wathu wa mapemphero, cikhulupiriro cathu cidzaonjezekeranso, ndipo Mulungu adzatidalitsa pamodzi ndi umboni wathu wa ci Kristu.

KUMALIZA:

Tsopano tiyeni tibwereze njira zina zomwe pemphero lingakhalire la tanthauzo m'miyoyo yathu. (Funsani mai aliyense mafunso, ndikuwapatsa nthawi yoyankha ndikukambirana, mwina kuonjezera maganizo ao. Tsimikizani kuti muli ndi yankho lokonzekeratu nthawi ya msonkhano isanafike.)

Tsekani msonkhano powerenga pamodzi pemphero la mu Mateyu 6:9-13 (mukhoza kulemberatu mapepala ena kuti mupatse mai aliyense opezekamo. M'njira yotero akhoza kutenga ndikukagwiritsa nchito kunyumba).

tifuna kukula monga Akristu amphamvu.

GAWO 3: KODI AKRISTU AMAPEMPHERERA CIANI?

Pamene ana adayamba kupemphera anali wosangalala ndi cipulumutso cace ndi cikondi ca Mulungu ca kwa iye kotero kuti adapitiriza kupemphera mapemphero a cithokozo. Iye adaona kwa nthawi yoyamba zinthu zonse zomwe Mulungu adamupatsa: moyo wabwino, mwamuna wabwino ndi ana, nyumba, mvula, nthaka, dzuwa lomwe linali kuthandiza mbeu kukula. Motero iye adathokoza Mulungu ca zimenezi.

Posacedwa adayamba kuzindikira kuti sanali kuyamikira kwa Mulungu nthawi zonse ndipo kawiri kawiri sanali kucita monga Mkristu. Motero ana adayamba kufunsa Mulungu kuti amuthandize pa umoyo wace wa tsiku ndi tsiku. Adapempha kuti amukhululukire cifukwa ca zolakwa zambiri za tsiku liri lonse.

Pamene anapitiriza kuphunzira zambiri za Mulungu ndi cikondi cace, anali kufunitsitsa kuti ena adziwe Mulungu wace. Motero anayamba kuwapempherera atate wace, amene anali wacikunja, mwana wace amene analibe cipembedzo, ana ace, kuti aphunzire za Yesu ndi kukhulupirira iye akadali a ang'ono.

Sipanapite nthawi kufikira adaona kusoweka kwa abwenzi ace ndi kwa anthu amene iye sanawadziwe. Motero anapemphera ndi mtima wolemera kuti Mulungu athandize anthu amenewa ndikumugwiritsa nchito mu njira iliyonse kufalitsa mau ace kuti onse awamve.



Pemphero:

Khalani ndi nthawi ya pemphero la cete kuti aliyense akonzenso mapangano ace a kwa Mulungu kuti akhale moyo wokondweretsa iye mphindi iliyonse ya tsiku ndi tsiku, ndiponso kukhala okhulupirika pa kabweredwe ka ku chalichi.

PHUNZIRO 6

MUTU WA PHUNZIRO: KUZAMA MWAUZIMU

MUTU WA LERO: KUPYOLERA M'MAPEMPHERO

MAU APAMTIMA: "Koma iwe popemphera, lowa m'cipinda cako, nutseke citseko cako, nupemphere Atate wako ali m'tseri, ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe."
Mateyu 6:6

MTSOGOLERI:

Tisanayambe kuona kufunika kwa pemphero tiyenera kufuna ciyanjano ceni ceni ndi Mulungu. Iye ndi Atate athu ndipo ife ndife ana ace. Kodi mumadziwa atate anu motani? Kodi mudayamba mwalankhula naye? Zoonadi, timamudziwa cifukwa tinakhala nao, tinalankhula nao, tinamvetsera kwa iwo pamene anali kutithandiza kukula kucokera ku ubwana kufika ku ukuru. Pamena munali wamng'ono kodi munali kumangolankhula pamene munali ndi atate anu? Sizotero, munali kukonda kumvetsera. Pamene munali kupita kwa iye kupeza cithandizo kapena ndi

bvuto, kodi munali kukhulupirira yankho lace?

Pemphero ndi kulankhula ndikuceza ndi Mulungu, atate wathu wakumwamba. Timafunika kupita kwa iye tsiku liri lonse m'mapemphero. Pamene tiri kupemphera, timalandira citsogozo mu nchito yathu ya tsiku ndi tsiku. Sikuti tingolankhula kwa iye, komanso tifunika kumvetsera modekha pamene ali kubvumbulutsa cifuniro cace ca pa miyoyo yathu pa ife. Lero tiyesa kuyankha mafunso a za pemphero - cifukwa, kuti, motani, ndi cifukwa ciani.

## GAWO 1: KODI NDI CIFUKWA CIANI AKRISTU AMAPEMPHERA?

Mu cipangano Catsopano timawerenga kucokera mu Mateyu 26 vesi 41 kuti tiyenera "kudikhira ndi kupemphera kuti tisalowe mu mayesero: mzimu zoonadi umafuna koma thupi ndi lofooka." Pali zifukwa zambiri zomwe ife tiyenera kupempherera. Timapeza mphamvu yokumana ndi mayesero a tsiku ndi tsiku popita kwa Atate m'mapemphero. Kupyolera m'moyo wa mapemphero opitiriza Mulungu akhoza kulankhula nafe ndi kutigwiritsa nchito muutumiki wace.

Beti anali kulankhula kwa mbusa wace. Iwo anali kulankhula za moyo wa mapemphero wace. Kwa masabata ambiri adadzipatulira nthawi ya mapemphero tsiku liri lonse. Iye anali wokondwa cifukwa adayamba kuona kudabwitsa kwace kuti kunali kotani polankhula ndi Mulungu kupyolera m'mapemphero. Iye adanena kuti. "Ciyambire comwe ndapita kwa Mulungu m'mapemphero, ndiri okondwera. Masiku anga ndi odzaza ndi cimwemwe ndi mtendere. Tsopano



ndiri ndi mphamvu yokumana ndi mabvuto anga ndi kukhala Mkristu wabwino. Ndisadayambe kumapemphera tsiku liri lonse, ndinali kuiwala kucita monga Mkristu. Koma tsopano pemphero ndi lofunika kwa ine motero kuti sindingaiwale."

## GAWO 2: KODI AKRISTU AMAPEMPHERERA KUTI?

Pamene Magret anali kugwira nchito m'munda mtima wace unali wolemera. Panali patangopita sabata zowerengeka pamene anaika mwana wace m'manda, koma anali kumusowabe kwambiri. Iye anayang'ana kumwamba m'mitambo yobiriwira ndikupemphera pamene anali kugwira nchito, "O Mulungu, ndiri wofooka. Koma inu ndinu wa mphamvu. Thandizeni nthawi ino yakusowa ndi yosikidwa." Kumunda kuli bata adaona mphamvu zatsopano. Iye anali Mkristu watsopano ndipo anaphunzira kwa nthawi yapitayo kuti akhoza kupemphera kwa Mulungu kuli konse.

Pamene Yohana adauka kunali kuli kwakudabe, ngakhale kuwala kunali kubwera kucokera ku m'mawa. M'mawa uli wonse anali kumauka banja lace lisanauke ndikupeza malo acete kunja kwa nyumba yace kukhala pansi ndi kupemphera kwa Mulungu. Iye adaphunzira Mateyu 6:6 amene auza Akristu kuti apeze malo otsekedwa kapena malo acete kulankhulana ndi Mulungu. Iye adaona kuti cimeneci ndicothandiza kwambiri. Pomacita zimenezi tsiku ndi tsiku, anali kulimbikitsidwa pa tsikulo.

Tikhoza kupemphera tokha, ndi ena, ku chalichi, ku nchito kapena kunyumba, koma tiyenera kukhala ndi dongosolo la mapemphero motero kuti tikhoza kulankhulana ndi Mulungu ngati